

Apolisi akonzeka kuthana ndi ziwawa zokhudza ndale



Achinyamata akufuna maudindo


Ulendo wa a Kondowe pa ndale

# 2025 ndi ifeyo

DEMOKALASE YOKOMERA ALIYENSE | VOL 01 | NO 01 LOWERUKA, 28 JUNI 2025

# ATSOGOLERI 14 AKUFUNA UPULEZIDENTI



## A Joyce Banda ndi amayi okhawo omwe akufuna kudzapikisana nawo

BRIGHT KUMWENDA

Pofika dzuro m'mawa, atsogoleri 14 ndiwo anatenga makalata kuchokera ku bungwe la Malawi Electoral Commission (MEC) ofuna kudzapikisana nawo pa mpando wa mtsogoleri wa dziko lino.

Chiwerengero cha onse omwe atenga kale makalata ndipo akufuna kudzayima ngati aphungu ndi makhansala sichikudziwika,

IKUPITIRIRA | PEJI 3

Mtalimanja: Tawonjezera nthawi

Embassy of Iceland Lilongwe

Funded by the European Union

**Kupititsa patsogolo ulamuliro wa amai, achinyamata ndi anthu aulumali m'Malawi**

## NDEMANGA

### Tiyeni tipewe ziwawa, nkhondo siimanga

**N'zomvetsa chisoni kuti pamene dziko la Malawi likukonzekera kudzavota pa 16 Sepitembala, ziwawa zikupitirira m'maboma ena a m'dziko muno.**

**Posachedwapa anthu osadziwika bwino adaotcha minibasi ya chipani cha Democratic Progressive Party (DPP) ku Mponela m'boma la Dowa pamene ku Ndirande m'boma la Blantyre, anthu ena adavulitsa amayi zovala za makaka a Malawi Congress Party (MCP) ndi kuwatsitsa m'minibasi yomwe adakwera.**

**Nkhani ngati izi n'zambiri. Malipoti ena adaperekedwa ku polisi, koma ena sadafike.**

**Tigwirizane ndi mafumu komanso a ndale omwe akuti ziwawa zimasokoneza zisankho, komanso kuchititsa amayi ndi anthu aulumali kuti aziopa kutenga nawo gawo pa zisankho.**

**N'zoona ziwawa n'zoipa posatengera kuti munthu yemwe akuzichita ali m'chipani cholamula kapena chotsutsa boma.**

**Ziwawa zilibe malo m'boma la demokalase lomwe limalimbikitsa ulamulilo wa zipani zambiri, komanso kulolerana pa ndale.**

**N'zosangalatsa kuti mkulu wa polisi a Merlyne Yolamu atsimikizira Amalawi kuti apereka chitetezo chokwanira m'misonkhano yokopa anthu, pokaponya mavoti, komanso poulutsa zotsatira za zisankhozo.**

**Izi ndi zotsangalatsa, komanso zomwe Amalawi ambiri amafuna, moti mabungwe a Oxfam, Women Legal Resource Centre ndi ena akhala akukumana ndi kukambirana ndi zipani za ndale komanso apolisi ubwino wa zisankho za bata ndi mtendere.**

**Tipemphe apolisi kuti azigwira ntchito yawo mwaukandaulo ndi kumanga aliyense woyambitsa ziwawa posatengera chipani kapena makaka a ndale womwe wavala.**

**Nkhondo siimanga mudzi! Udindo wosungitsa bata ndi mtendere ndi wa tonse!**

**Choncho tiyeni tigwirane manja pokana ziwawa ndi mtopola uliwonse womwe ungadzetse mpungwepungwe pa ndale.**

MKONZI

**Phone: (+265) 888 20 90 27/0999 91 26 79**
**Email: brightkumwenda.npl@gmail.com**

# Kuunika za Simatimatiki

LUCKY MKANDAWIRE

Mtsutso wabuka pakati pa zipani zotsutsa boma ndi bungwe loyendetsa zisankho m'dziko muno la Malawi Electoral Commission (MEC) pa nkhani yogwiritsa ntchito Simatimatiki.


Simatimatiki, malingana ndi wapampando wa bungwe la MEC a Annabel Mtalimanja, ndi dongosolo logwiritsa ntchito makina a makono polemba ovota m'kaundula wa zisankho komanso potumiza zotsatira.

Simatimatiki ndi chidule cha mawu a Chingerezi otchedwa Smartmatic Election Management System (EMS).

Zipani zotsutsa boma sizikufuna kuti Simatimatiki idzagwire ntchito pa zisankho za pa 16 Sepitembala poganiza kuti ena atha kudzatengerapo mwayi wobera zisankhozo.

Mlembi wa chipani cha Democratic Progressive Party (DPP) a Peter Mukhito apempha kuti mndandanda wa maina ovota uwunikidwenso kaamba koti Simatimatiki idagwiritsidwa ntchito, komanso dongosololi lisadzagwire ntchito potumiza zotsatira za zisankhozo.

DPP ndi zipani zina zitatu zidapereka kale ku MEC magawo a Simatimatiki omwe akufuna kuti awaunike, koma mneneri wa MEC a Sangwani



**Kondowe:** Tiwononga ndalama

Mwafulira akuti bungwe lawo lakana pempholo..

MEC idaganiza zosintha dongosolo lolembetsera maina m'kaundula wa zisankho ndi kutumiza zotsatira zake atakaona momwe dziko la South Africa ndi Zambia adayendetsera zisankho zawo pogwiritsira ntchito Simatimatiki.

Kuchokera nthawi imeneyo, MEC yakhala ikukambirana ndi zipani za ndale ndi mabungwe moti nthumwi zina zidapita ku Zambia kukaphunzira za Simatimatiki.

Onse atagwirizana, MEC idagula makina 6 500 olembetsera maina m'kaundula ndi kutumizira zotsatira za zisankho.

Atafika makinawo pa bwalo la ndege la Kamuzu International Airpot, akuluakulu a zipani za ndale ndi mabungwe adaitanidwa kuti akachitire umboni.

Mwadzidzidzi, MEC idadabwa kuti akuluakulu a zipani za ndalezo asintha maganizo awo zomwe katswiri wina wa za malamulo, yemwe sadafune kuti dzina lake litchulidwe, adati n'kulakwa chifukwa onse akhala akuyendera limodzi mpaka kudzafika pogula makinawo.

Wapampando wa bungwe la Civil Society Elections Integrity Forum a Benedicto Kondowe adati kusintha kwa dongosolo lolembetsera ndi kutumizira zotsatira za zisankho kutha kuonongetsa dziko lino ndalama zambiri.

Mmbuyomu a Mtalimanja adauza dziko lino kuti ndalama zoyendetsera zisankho zaperewera ndi K97.9 biliyoni.


Malingana ndi mkuluyu, MEC idapempha K220 biliyoni yoti iyendetsere zisankho za pa 16 Sepitembala.

"Mmalo mouza MEC kuti isagwiritse ntchito Simatimatiki zipani zotsutsa boma zingokambirana ndi MEC ndi cholinga chofuna kuchotsa nkhawa zawo," atero a Kondowe.

Zipani zotsutsa zikuti m'maiko omwe adagwiritsa Simatimatiki pa zisankho monga Kenya, Venezuela ndi Phillipines zotsatira zake zidali zosadalirika, koma a Mtalimanja akuti izi ndi nkhambakamwa chabe.

MEC ikuti igwiritsabe ntchito Simatimatiki, koma nazo zipani zotsutsa zatemetsa nkhwangwa pa mwala kuti sizitheka.

## Mayi Chisankho



# Apolisi akonzeka kuthana ndi ziwawa zokhudza ndale

KANDANI NGWIRA ndi BRIGHT KUMWENDA

Apolisi akuti apereka chitetezo chokwanira m'misonkhano yokopa anthu, povota komanso potulutsa zotsatira za chisankho cha pa 16 Sepitembala.

Mkulu wa polisi a Merlyne Yolamu ndiwo adalankhula izi pa msonkhano omwe bungwe la Public Affairs Committee (PAC) lidachititsa posachedwapa mu mzinda wa Blantyre.

"Tamva madandaulo a Amalawi okhudza ziwawa ndipo ndikufuna ndikutsimikizireni kuti tikuchita zotheka kuti tikhale ndi zisankho za mtendere," iwo adatero.

Pothirirapo ndemanga, mkulu wa bungwe la Centre for Democracy and Economic Development (CDEDI) a Silvester Namiwa ndi wa Human Rights Defenders Coalition (HRDC) a Gift Trapence adadzudzula apolisi kuti akulekerera ziwawa za ndale.

"Ife tikuona kuti apolisi athu akulekerera ziwawa chifukwa sakumanga anthu omwe adachita za mtopola ku Mponela ndi ku Ndirande ngakhale anthuwo




**Yolamu:** Takonzekera bwino zisankhozi

ali odziwika," adatero a Trapence.

A Mary Navicha, a chipani cha Democratic Progressive Party (DPP), adagwirizana ndi a Namiwa komanso a Trapence.

"Mpaka pano apolisi sadagwirebe anthu omwe adaphwetsa matayala a galimoto za aphungu a Nyumba ya Malamulo," iwo adatero.

Posachedwapa anthu osadziwika adavulitsa amayi nsalu za makaka a Malawi Congress Party (MCP) ndi kuwatsitsa m'minibasi ku Ndirande mu mzinda wa Blantyre pamene ku Mponela m'boma la Dowa anthu ena adaotcha minibasi ya chipani cha DPP.

Poyankha, a Yolamu adati apolisi amatengerapo kanthawi pang'ono kumanga anthu omwe akuwaganizira kuti apalamula mlandu ndi cholinga choti apeze umboni wogwirika.

Ngakhale ziwawa zikupitirira, mkulu wa polisi watsimikizira Amalawi kuti asade nkhawa popeza akonzekera mokwanira kuthana ndi mpungwepungwe uliwonse womwe ungadze pa nthawi ya zisankho.

A Yolamu adaonjezera kuti akhala akukumana ndi akuluakulu a zipani, a mabungwe ndi a mipingo n'cholinga chopeza njira zothetsera ziwawa za ndale.

Mkulu wa Oxfam a Lingalireni Mihowa adatsimikiziza kuti bungwe lawo lakhala likukumana ndi apolisi n'cholinga chofuna kupeza njira zothana ndi ziwawa za ndale m'dziko muno.

Mmodzi mwa akuluakulu a bungwe la Federation of Persons with Disabilities in Malawi (FEDOMA) a Ethel Kachala adati ziwawa za ndale zichititsa kuti amayi ndi anthu aulumali asatenge nawo gawo pa ndale.

Bungwe la Nation Youth Council lidachenjeza zipani za ndale kuti zilekeretu m'chitidwe wogwiritsa ntchito achinyamata pa ziwawa za ndale.

AYAMBA KANDODO NDI BRIGHT KUMWENDA

# Mafumu akulimbikitsa amayi

Mafumu akufuna amayi, achinyamata ndi anthu aulumali ambiri atenge nawo gawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala.

Polankhula ndi nyuzipepala ya 2025 Ndi Ifeyo, a mfumu a Chowe a ku Mangochi alonjeza kuti apempha nyakwawa ndi mafumu onse a m'bomalo kuti alimbikitse amayi, achinyamata ndi anthu aulumali kudzaima nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembara.

A Victoria Kingstone, omwe akufuna kudzaimira dera lapakati pa boma la Mangochi, adauza msonkhano womwe bungwe la Civil Society Strengthening (CCSS) lidachititsa m'bomalo kuti anthu ena akutukwana ndi kulankhulira mawu achipongwe amayi.

"Izi zimabwezera mmbuyo maloto athu pa ndale ndi kugwetsa mphwayi amayi ambiri omwe akufuna kulowa ndale," iwo atero.

Pothirirapo ndemanga, a Chowe akuti n'zomvetsa chisoni kuti amayi omwe akufuna kupikitsana nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala akukumana ndi mikwingwirima ndipo adaopseza kuti athana ndi aliyense wochita izi.

"Ndikumana ndi mafumu komanso nyakwawa zanga kuti akhale tcheru ndi kupereka chindapusa kwa aliyense wochitira amayi mtopola m'madera mwawo," alonjeza choncho a mfumuwo.

A mfumu a Kachindamoto a m'boma la Dedza ndi a mfumu a Kameme a m'boma la Karonga adzudzula anthu omwe akuchitira amayi ndi anthu aulumali mtopola.

"M'dera langa lino ndidawauziratu kuti amayi ndi anthu aulumali ali ndi ufulu wopikisana pa mpando uliwonse wa ndale ndipo sindikufuna



**Kachindamoto:** Amayi ali ndi ufulu wochita ndale

wina kuwatukwana kapena kuwachita chipongwe," atero a Kachindamoto.

Nawo a mfumu Chikulamayembe a m'boma la Rumphi akuti ndi ufulu wa amayi, achinyamata ndi anthu aulumali kuchita nawo ndale.

"Sindidzalola aliyense kuphwanya ufulu wa amayi, achinyamata ndi anthu aulumali m'dera langa," iwo adatero.

A mfumu Jalavikuba a m'boma la Mzimba ndi a mfumu a Kameme a m'boma la Karonga alimbikitsa amayi kutenga nawo gawo pa ndale.

"Abambo tawayetsa, koma taona tokha kuti zikuwakanika. Choncho ndi nthawi yoti amayi akhale ndi mwayi wotenga gawo pa ndale," iwo adatero.

Katswiri wa za ndale wa ku sukulu yaukachenjede ya Malawi University of Business and Applied Sciences (MUBAS) a Chimwemwe Tsitsi apempha mafumu kuti agwirane manja ndi zipani za ndale kuti chiwerengero cha amayi chikwere m'Nyumba ya Malamulo.

Mwa aphungu 193 omwe ali m'Nyumba ya Malawi aphungu 40 okha ndi amayi.



**Mwafulirwa:** Panopa sizikudziwika

## Atsogoleri 14 akufuna upulezidenti

YACHOKERA | PEJI 1

malingana ndi mneneri wa bungwelo a Sangwani Mwafulirwa.

Padakali pano mtsogoleri wa dziko lino komanso wa chipani cha Malawi Congress Party (MCP) a Lazarus Chakwera ndi a Peter Mutharika a Democratic Progressive Party (DPP) adatenga kale makalata awo.

Atsogoleri ena omwe atenganso makalata awo ndi a Joyce Banda a People's Party, a Atupele Muluzi a United Democratic Party, a Dalitso Kabambe a UTM, a Kamuzu Chibambo a People's Transformation Party, a Frank Mwenifumbo a National Development Party, a David Mbewe a Liberation for Economic Freedom Party, a Kondwani Nankhumwa a People's Development Party, komanso a Kwame Bandawe a chipani cha Anyamata, Atsikana, Amayi.

A Milward Tobias, Hardwick Kaliya, Adil Chilungo ndi a Smart Swira adzaima paokha pa chisankhochi.

Padakali pano a Joyce Banda ndi mayi yekhayo yemwe akufuna kudzapikisana nawo pa chisankhozi cha mtsogoleri wa dziko lino.

Pothirirapo ndemanga, katswiri wa ndale wa ku Malawi University of Business and Applied Sciences a Chimwemwe Tsitsi wati zomwe zikuchitika m'dziko muno sizachilendo.

"Ngakhale m'maiko a ku Ulaya si amayi ambiri omwe amapikisana

IKUPITIRIRA | PEJI 5

# Amayi apatsidwe mwayi pa ndale

Mabungwe a Oxfam ndi Women and Legal Resource Centre (WOLREC) akuthandiza amayi, achinyamata ndi anthu aulumali omwe akufuna kudzapikisana nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala 2025. MACMILLAN MHONE adacheza ndi mkulu wa bungwe la Oxfam a Lingalireni Mihowa kuti amve zambiri:

**Tafotokozani mwachidule ntchito zokhudza zisankho za pa 16 Sepitembala 2025 zomwe mabungwe a Oxfam ndi WOLREC akugwira.**

Malamulo a dziko lino amati amayi ali ndi ufulu wokwaniritsa zofuna zawo pa ndale. Tilinso ndi ndondomeko zolimbikitsa utsogoleri wa amayi pa ndale. Kwa zaka zingapo, takhala tikupanga kampeni yolimbikitsa amayi kutenga nawo gawo pa ndale yotchedwa 50:50. Pamene tikuyandikira zisankho za mu Sepitembala chaka chino, tikupereka upangiri wothandiza amayi omwe akufuna kuima nawo pa mipando ya ukhansala ndi uphungu wa ku Nyumba ya Malamulo.

**Kodi n'chiyani chomwe mukufuna kukwaniritsa?**

Tikufuna kulimbikitsa amayi kuima nawo pa zisankho za mu Sepitembala, komanso kukhala patsogolo pa ndale. Tikufuna kukwaniritsa ndondomeko yomwe boma la Malawi lidakhazikitsa yoti mwa makhansala ndi aphungu 100 alionse omwe adzasankhidwe, 35 adzakhale amayi.

**Mwakhazikitsa ndondomeko zotani zothandiza kukwaniritsa zolinga zanu?**

Mu 2023, ifeyo a Oxfam ndi a WOLREC tidakumana ndi amayi omwe akufuna kulowa ndale ndipo adatiuza kuti akusowa upangiri kuchokera kwa amayi omwe ndi mkhalakale pa ndale. Adatipatsa maina a amayi omwe amafuna kuti adzawapatse upangiriwo. Pachifukwa ichi, m'maphunziro omwe takhala tikuchititsa takhala tikuitana mkhalakale pa ndale monga a Patricia Kaliati, Mary Navicha, Catherine Gotani-Hara, Esther Jolobala ndi a Rachel Zulu kuti asule amayi anzawo.

**Ndi magulu ati omwe akuyembekezera kupindula ndi ntchitozi?**

Maphunzirowa tikupereka kwa amayi omwe akufuna kudzaima nawo pa mipando ya ukhansala ndi uphungu wa ku Nyumba ya Malamulo.

**Kodi iwowa apindula motani?**

Amayiwa akulandira upangiri kuti kudziwe zinthu zofunika pa ndale, komanso zoyenera kuchita kuti adzapambane pa zisankho za pa 16 Sepitembala. Amayi omwe adzalandire chiphaso kuchokera ku bungwe loyendetsa zisankho la Malawi Electoral Commission (MEC) chowalola kudzapikisana nawo pa zisankhozo, tidzawapatsa zinthu zowathandiza kuchititsa misonkhano yokopa anthu. Tikuyetsetsa kuti amayi tawafikire kwa nthawi yaitali.

**N'chiyani chomwe amayi akuyenera kuchita kuti apindule nawo?**

Padakali pano Oxfam ndi WOLREC akulangiza amayi kuti akhale olimba mtima, odziwa kucheza ndi anthu a m'madera mwawo, komanso tikuwapatsa luso la mmene angadziwire zofuna za anthu, komanso ukadaulo wapadera wa mmene angaperekere mauthenga okopa anthu m'misonkhano yawo. Mabungwewa athandizanso amayi kudziwa malamulo oyendetsera zisankho a dziko lino kaamba koti adasintha.

Mukugwira ntchito motani ndi bungwe la MEC?

A MEC tidawafotokozera zomwe tikuchita ndi zolinga zake ndipo adatipatsa chiphaso chotilola kumemeza anthu pa nkhani zokhudza zisankho, komanso kuyendera malo oponyera voti.

Tidakumananso ndi wapampando wa MEC a Annabel Mtalimanja n'kuwapempha kuti ndalama zomwe amayi amalipira ku bungwe lawo akafuna kupikisana nawo azitsitse ndipo pempho lathu lidamveka kaamba koti amayi apereka ndalama zocheperako poyerekeza ndi abambo.

**Ndi ntchito ziti zomwe mabungwe anu akwaniritsa kale?**

Tachititsa kale maphunziro a amayi m'zigawo zonse za m'dziko lino. Tafikira mafumu n'kuwapempha kuti alimbikitse amayi a m'madera awo kuti atenge nawo gawo pa ndale. Tachititsa misonkhano ndi amayi, apolisi ndi atsogoleri azipembedzo zosiyanasiyana.

**Rwanda, South Africa ndi Namibia ndi ena mwa maiko omwe akuchita bwino poonetsetsa kuti amayi akutenga nawo maudindo a ndale. Kodi anzathuwa adagwiritsa ntchito ndondomeko zotani zoti ife tiphunzire nawo?**

Maiko a anzathuwa amaperekeratu mipando ina kuti ikhale ya amayi. Kutsogoloku dziko la Malawi likufunika liikenso ndondomeko zofanana ndi za anzathuwa. M'mbuyomu nkhaniyi idakambidwapo koma siidafike popanga lamulo loti aphungu a ku Nyumba ya Malamulo aliunike. Pachifukwa ichi, tikuthamangabe pogwiritsa ntchito malamulo omwe tili nawo.

Tafotokozani mwatsatanetsatane mavuto omwe amayi akukumana nawo.

Akusowa upangiri wa mmene angachitire kampeni, ndalama zolipira pa zisankho, komanso ziwawa zikubwezera mmbuyo ntchito yolimbikitsa amayi kutenga gawo pa ndale. Amayi akukumana ndi zotsamwitsa zosiyanasiyana pa zisankho za chipulula za m'zipani.

**Mukuthana nawo bwanji mavutowa?**

Takhala tikukumana ndi zipani kuti apange ndondomeko zoti amayi asapsinjike pa zisankho za chipulula. Ndife okondwa kuti zipani zina zidamvera ndipo zidaika ndalama zocheperapo zoti amayi azilipira akafuna kuimira.

Pa nkhani ya ziwawa, takhala tikukambirana ndi atsogoleri a zipani za ndale, komanso mkulu wa polisi a Merlyne Yolamu kufunika kopeza njira zothetsera ziwawazo. Amayi omwe akufuna kudzaima pa zisankho za pa 16 Sepitembala adawafotokozera a Yolamu mavuto omwe akukumana nawo ndipo iwo adalonjeza kukhazikitsa komiti yapadera yoti ipeze njira zothana ndi ziwawa zokhudza ndale.

**Mawu anu owonjezera?**

Amayi 40 omwe alipo pano ngati aphungu a ku Nyumba ya Malamulo achita bwino ndipo apereka upangiri wofunikira pa chitukuko cha dziko lino. Nawo makhansala athu achitanso bwino ndipo ena adasankhidwa kukhala mafumu a mizinda ya m'dziko muno. Izi zimatipatsa mangolomera kuti zinthu zikuyenda, ndipo amayi akuchita bwino. Ife tikuona kuti nthawi yakwana yoti tipereke mwayi wokwanira woti amayi adzapikisane nawo pa zisankho za mu Sepitembala.



**Mihowa:**: Chiwerengero cha amayi, achinyamata ndi anthu aulumali chikwere

# MCP, DPP ilipirira amayi osowa ku bungwe la MEC

BRIGHT KUMWENDA

Zipani za Malawi Congress Party (MCP) ndi Democratic Progressive Party (DPP) zilipirira amayi omwe achite bwino pa zisankho za chipulula, koma akulephera kupereka ndalama zomwe bungwe la Malawi Electoral Commissionm (MEC) likufuna kuti awalowetse m'kaundula wa anthu odzapikitsana nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala.

Patsikulo anthu adzaponya mavoti osankha mtsogoleri wa dziko lino, aphungu a Nyumba ya Malamulo ndi makhansala.

Pocheza ndi mtolankhani wa wailesi ya kanena ya Times a Brian Banda, mlembi wa MCP a Richarda Chimwendo-Banda adati chipani chawo chilipirira amayi omwe sakwanitsa kudzilipirira kuti alowe m'kaundula ya anthu odzapikitsana nawo ya MEC.

"Tidzalipirira amayi onse omwe sakwanitsa kulipira okha, koma ali ndi kuthekera kodzachita bwino pa zisankho za pa 16 Sepitembala.

"Sitikufuna kuneneratu poyera poopa kupereka mwayi kwa anthu ena omwe ali ndi kuthekera kodzilipira," anatero Chimwendo-Banda.

Nawo a Mary Navicha, mkulu wa amayi mu Democratic Progressive Party (DPP), akuti chipani chawo chakonza ndondomeko yolipira amayi omwe sakwanitsa kudzilipirira ku MEC.



**Chimwendo Banda:** Tilipirira okhawo omwe sangakwanitse kulipira paokha

Aliyense yemwe akudzaima nawo pa zisankho akuyenera kulipira ku MEC kuti alowe m'kaundula wa anthu odzapikitsana nawo pa zisankhozo.

Anthu omwe akudzapikitsana pa chisankho cha mtsogoleri wa dziko lino adzalipira K10 miliyoni aliyense pamene abambo omwe akudzapikitsana pa mpando wa aphungu a Nyumba ya Malamulo adzalipira K2.5 miliyoni pamene amayi, achinyamata ndi anthu aulumali adzalipira K1 500 000 lomwe ndi theka la ndalamazo.

Abambo omwe akudzapikitsana pa undindo wa makhansala adzalipira K200 000 pamene amayi adzalipira K100 000.

Mabungwe a Oxfam ndi Women Legal Resource Centre (WOLREC) akhala akukambirana ndi MEC komanso zipani za ndale kuti atsitse ndalama zomwe amayi, achinyamata ndi anthu aulumali omwe akufuna kudzapikitsana nawo pa zisankho adzapereke.

"Tidapempha anzathu a MEC kuti atsitse ndalama zomwe amayi azilipira ndipo adatimvera," atero a Lingalireni Mihowa, mkulu wa bungwe la Oxfam.

Zipani zambiri za ndale zidamvera pempholo moti amayi, achinyamata ndi anthu aulumali omwe akupikitsana pa zisankho za chipulula za m'zipani apereka theka la ndalama zomwe abambo akulipira.



A Joyce Banda apereka kale makalata awo

## A Joyce Banda akufuna kuimira upulezidenti

YACHOKERA | PEJI 3

nawo pa mpando wa pulezidenti," iwo atero.

Katswiriyu akuti m'boma la demokalase zipani za ndale ndizo gwero la maudindo onse.

"Dziko la Malawi limatsatira boma la demokalase lomwe limapereka mphamvu kwa osatira zipani, kudzera m'misonkhana yawo ikuluikulu, kusankha atsogoleri omwe akufuna adzawayimire pa chisankho cha pulezidenti monga chomwe tikhale nacho pa 16 Sepitembala.

"Choncho amayi ayenera kupatsidwa mpata wopikisana nawo m'maudindo akuluakulu kuphatikizirapo woimira zipani zawo ngati pulezidenti wa dziko," atero a Tsitsi.

Akuluakulu a zipani za MCP, DPP ndi UTM, omwe sadafune kutchulidwa maina, akuti sakudziwa anthu omwe adzaimire limodzi ndi atsogoleri awo (runningmates).

Wapampando wa MEC a Annabel Mtalimanja apempha aliyense yemwe akufuna kudzachita nawo zisankhozi kuti alipiriretu asadatenge makalata ku bungwe lawo. "Ndikudziwitsa zipani za ndale ndi anthu omwe akufuna kudzaima pa mipando yosiyanasiyana kuti MEC yaonjezera nthawi yopereka makalata" iwo adatero.

A Mtalimanja akuti anthu omwe akudzapikisana pa mipando yosiyanasiyana ayenera kudzapereka zikalata zawo kuyambira pa Julaye 24 mpaka 30.

# WOMEN yakhazikitsa manifesito

BRIGHT KUMWENDA



Akatswiri omenyera ufulu wa amayi akuti manifesito ya amayi ndi chida cha mphamvu chosinthira moyo wawo pa ndale m'dziko muno.

Akatswiriwa adalankhula izi pa mwambo wokhazikitsa manifesito ya amayi womwe udakonzedwa ndi Women's Manifesto Movement (WOMEN) ku Lilongwe.

Polankhula pamwambowo, katswiri womenyera ufulu wa amayi wa m'dziko la South Africa a Dr Naledi Pandor adayamikira WOMEN pokhazikitsa manifesitoyo.

"Manifesitowa ndi dongosolo lozama lofotokoza zomwe amayi a m'dziko muno akufuna.

"Mukawerenga modekha mumva kuti amayi akufuna akhale aphungu a Nyumba ya Malamulo, nduna za boma, komanso kutenga nawo gawo m'madera onse achitukuko," adatero a Pandor.

Katswiriyu adaunikira mozama moyo wa Charlotte Maxeze, mayi wodziwika bwino pa nkhani yomenyera ufulu ku South Africa ndi kuwalimbikitsa amayi m'dziko muno kuti achilimike pofuna kukwaniritsa ufulu wawo.

A Pandor ndi mphuzitsi, akhalapo nduna ya boma m'dziko la South Africa, komanso kazembe wa amayi ku United Nations.

Mkulu wa bungwe la Women Legal Resource Centre (WOLREC) a Maggie Kathewera-Banda akuti manifesito ya amayi ndi dongosolo lakuya la mfundo zomwe amayi akufuna zikwaniritsidwe kuti moyo wawo pa ndale ndi pa chitukuko usinthe.

Mkulu wa bungwe la Oxfam a Lingalireni Mihowa adati manifesito yoyamba idapangidwa mu 2018 koma idakhazikitsidwa mu 2019.

"Taganiza zoyisintha ndi kuyikhazikitsanso kaamba ka kusintha kwa zinthu m'dziko muno komanso m'maiko ena," iwo adatero.

Manifesitoyo ikuunikira ufulu wa amayi wochita ndale, kukhala ndi katundu, malo, kugwira ntchito zofanana ndi abambo ndi zina zomwe WOMEN ikufuna atsogoleri ndi zipani zawo za ndale ziwunike mozama pamene zisankho za pa 16 Sepitembala zikuyandikira.

"Tikufuna atsogoleri a ndale ndi zipani zawo ayike m'manifesito awo mfundo zomwe zili m'manifesito a amayi n'kutiuza momveka zomwe adzachite akasankhidwa pofuna kukwaniritsa mfundozo.

"Tikufuna zofuna za amayi zidziwike ndi aliyense. Pamapeto pa zonse tikufuna kuona amayi akutenga gawo m'madera osiyanasiyana a chitukuko," atero a Kathewera Banda.

WOMAN yapangidwa ndi mabungwe osiyanasiyana monga a Oxfam, Women Legal Resource Centre (WOLREC), Gender-Coordination Network, Hivos, UN ndi ena ambiri.

**A Kathewera Banda:** Andale ayigwiritse ntchito

# Achinyamata akufuna maudindo

JACOB NANKHONYA



Achinyamata, mkulu wa makhoti, nduna ya zachuma ndi Sipika kuonetsa manifesitowo

Mtsogoleri wa bungwe la Youth and Society a Charles Kajoloweka asindika kufunika kokhazikitsa malamulo okakamiza boma kuti lizipereka maudindo ena akuluakulu kwa achinyamata.

Iwo alankhula izi Lachitatu mu mzinda Lilongwe komwe achinyamata amakhazikitsa manifesito yawo n'cholinga choti yiunikire atsogoleri ndi zipani za ndale pamene zikukonza ma manifesito awo a zisankho za pa 16 Sepitembala.

Iwo adati malamulo a dziko lino amateteza ufulu wa amayi ndi anthu aulumali, koma safotokoza molunjika zokhudza achinyamata.

"Padakali pano tilibe malamulo, mwachitsanzo, okakamiza boma kuti mwa maudindo 100 alionse 30 azipite kwa achinyamata.

"Manifesito ya achinyamata ndi mlozo womwe mtsogoleri wa dziko lino yemwe timusankhe pa zisankho za pa 16 Sepitembala adzagwiritse ntchito posankha maunduna, komanso anthu otsogolerera madipatimenti ndi mabungwe aboma," adatero a Kajoloweka.

Iwo adati bungwe lawo ligwiritsa ntchito manifesitoyo pokhambirana ndi atsogoleri a ndale omwe akufuna kuti achinyamata adzawavotere pa zisankho zikudzazi.

Pothirirapo ndemanga, mkulu wa bungwe la United Nations m'dziko muno a Rebeccah Ada Donto adati kupereka mphamvu kwa achinyamata n'koyenera potengera ndi chiwerengero chawo.

"Koma msonkhanowu sukuunika za chiwerengero cha achinyamata chokha, komanso za ufulu ndi kuthekera kwawo," iwo adatero.

Ada Donto adati achinyamata si atsogoleri amawa okha, komanso a lero.

"Achinyamata ali ndi maluso komanso kuthekera kugwira ntchito zosiyanasiyana zotukula dziko lino," iwo adatero.

A Mwandida Theu, mmodzi mwa akuluakulu a kampeni ya Youth Decide, adapempha atsogoleri andale kuti awerenge manifesitoyo kuti adziwe zomwe achinyamata a m'dziko muno akufuna ndi kuzilingalira kwambiri popanga ma manifesito a zipani zawo.

"Mwa anthu 100 alionse omwe ali m'dziko muno, 60 ndi achinyamata. Kuphatikizira apo, kaundula wa zisankho akuonetsa kuti mwa anthu 100 alionse omwe adalembetsa, 63 ndi achinyamata.

"Choncho achinyamata akuyenera kutenga gawo lalikulu m'zipani, m'madipatimenti, maunduna ndi mabungwe a boma kuti dziko lino lipite patsogolo," iwo adatero.

Sipikala wa Nyumba ya Malamulo, a Catherine Gotani Hara adapempha achinyamata kuti achilimike pomenyera ufulu wawo.

"Musatope, musabwerere mmbuyo pomenyera ufulu wanu. Aphungu akangosankhidwa, akumbutseni zomwe mukufuna.

"Ndanena izi chifukwa mmene timatsiriza kukumana kwathu kwa Nyumba ya Malamulo palibe phungu amene adatulutsa nkhani yokhudza achinyamata.

"Ichi n'chifukwa sitidakambirane zokhudza achinyamata," iwo adatero.

# Achinyamata sakufooka, sakubwerera mmbuyo

MARTIN GERA JNR NDI BRIGHT KUMWENDA

Achinyamata, omwe adzapikitsana nawo pa zisankho za makhansala ndi a phungu a Nyumba ya Malamulo pa 16 Sepitembala, maso awo ali patsogolo, sakufooka, komanso sakubwerera mmbuyo.

A Eliza John, omwe akudzaima pa mpando wa khansala wa dera la Mbonechela m'boma la Machinga, ali pakalikiliki kuchititsa misonkhano n'cholinga choti anthu a m'dera lawo adziwe mfundo zawo za chitukuko.

"Masomphenya anga ndikubweretse zitukuku za madzi aukhondo, maphunziro, ulimi wamakono, komanso kutukula ntchito zaumoyo m'dera lathu," iwo atero.

A Hastings Mapundi, omwe akudzaima pa udindo wa phungu wa dera la pakati la m'boma la Nsanje, nawo maso awo ali patsogolo.


**Chambo:** Achinyamata anzanga achilandira


**Adam:** Ndibweretsa chitukuko

"Maso anga ali patsogolo. Sindikucheukanso kuopa kuphonyana ndi mpando wa phungu wa Nyumba ya Malamulo," iwo atero.

A Mapundi akufuna kudzathana ndi umphawi, ulova ndi njala zomwe zamanga mthenje m'deralo.

"Anthu ambiri m'dera lino ndi alimi. Choncho ndikufuna kutukula ulimi wothirira, kupeza misika yodalirika ya mbewu, kutukula bizinesi zing'onozing'ono, kupititsa patsogolo maphunziro a ntchito za manja. Izi zidzathandiza kuthetsa umphawi, ulova ndi njala m'dera lathu," iwo atero.

Masophenya awo sakusiyana ndi a Benjamin Kachikho Simeon, omwe akudzapikitsana nawo pa mpando wa phungu wa m'dera la Thyolo Thava.

"Ndikufuna kuthana ndi mavuto omwe anthu a m'dera lathu akukumana nawo. Ndikadzatenga mpando ndidzalimbikitsa ntchito za manja, bizinesi zing'onozing'ono, ulimi wothirira, masewero ndi maluso osiyanasiyana pakati pa achinyamata," iwo atero.

A Aaron Chambo, nawo sakubwerera mmbuyo, akufuna mpando wa phungu wa dera la pakati la boma la Mulanje.

"Ndikatenga mpando ndizapereka mphamvu kwa anthu, kudzetsa chitukuko zosiyanasiyana ndi kuchita zinthu poyera," iwo atero.

A Chambe akuti achinyamata ambiri "achilandira ndipo ali pambuyo pawo nga nga nga chifukwa masomphenya anga akugwirizana ndi awo".

Iwo akuti anthu a m'dera lawo akufuna zitukuko za maphunziro, zipatala, madzi aukhondo ndi misewu yabwino.

"Umphawi ndi ulova wakula kwambiri m'dera mwathu ndipo ndakonzeka kuthana nazo," atero a Chambo.

A Aida Adam Kunje, womwe akudzaima ngati khansala m'dera la Sankhwi ku Machinga, apempha anthu kuti awone zitukuko zomwe achita kale m'deralo.

"Anthu ndi mboni kuti ndayambitsa zitukuko za milatho, mijogo, magetsi ndi zina zambiri," iwo atero.

Ngakhale izi zili chonchi, achinyamata apempha Oxfam ndi Women Legal Resource Centre (WOLREC) kuti awathandize ndi zipangizo zokopera anthu ovota.

Oxfam ndi WOLREC akulimbikitsa achinyamata, amayi ndi anthu aulumali ambiri kuti apikitsane nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala.

Mkulu wa Oxfam a Lingalireni Mihowa alonjeza kuti adzawapatsa zipangizo zokopera anthu akalembetsa m'kaundulu wa bungwe la Malawi Electoral Commission (MEC) wa anthu omwe akufuna kudzapikitsana nawo pa zisankho.

A Mphatso Kapito, omwe akudzaima pa mpando wa phungu wa dera la kummwera chakumvuma kwa boma la Machinga, athokoza Oxfam ndi WOLREC chifukwa cha ntchito yotamandika yomwe akugwira.

"Oxfam ndi WOLREC akugwira ntchito yotamandika chifukwa akutilimbikitsa mtima, komanso kutiphunzitsa mmene tingakopere anthu a m'madera mwathu," iwo atero.

# Ulendo wa a Kondowe pa ndale

LOVEMORE KHOMO

Phungu wa Nyumba ya Malamulo wa dera la kumpoto cha kumvuma kwa boma la Nkhotakota a Overstone Kondowe akuti ulendo wawo pa ndale udali wozuna ndipo alimbikitsa anthu aulumali ambiri kuti adzapikisane nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala.

Iwo auza nyuzipepala ya 2025 Ndi Ifeyo kuti nthawi yomwe akhala m'Nyumba ya Malamulo yawasimikiza kuti palibe kusiyana pakati pa munthu waulumali ndi walungalunga pa ndale.

A Kondowe ndi munthu woyamba wa chialubino kukhala phungu wa Nyumba ya Malamulo m'mbiri ya dziko lino.

Mkuluyu adasankhidwa kukhala phungu nthawi yamikwingwirima yomwe anthu achialubino amadulidwa ziwalo, komanso kuphedwa m'dziko muno.

"Mavuto omwe anthu achialubino amakumana nazo sanandibwezere m'mbuyo, koma adandipatsa mangolomera woima ngati phungu.

"M'nyumba ya Malamulo ndakhala ndikulankhula kwambiri za anthu aulumali makamaka mavuto omwe amakumana nawo, kuthekera kwawo, komanso zomwe boma lingachite pofuna kuthana ndi mavuto awo," atero a Kondowe.

Iwo afotokoza kuti kusankhidwa kwawo kukhala phungu ndi umboni woti anthu aulumali ali ndi kuthekera ngati munthu wina aliyense.

A Kondowe akuti ubale wawo ndi aphungu achipani chawo cha Malawi Congress Party (MCP), komanso a zipani zotsutsa boma uli bwino kwambiri.

"Aphungu anzanga amanditenga ngati wina aliyense. Timacheza opanda kusalidwa kapena kulankhulidwa mawu achipongwe," afotokoza choncho phunguyu.

A Kondowe adasankhidwa mu 2021 potsatira imfa ya yemwe adali phungu wa deralo a Martha Lunji.

"Zitukuko zomwe a Lunji adasiya ndapitiriza ndi kutsiriza chifukwa zinali zofunika kwambiri kwa anthu a m'deralo.

"Anthu a ku Bua mpaka ku Dwangwa analibe madzi a m'mipope kupatula a pa Misson ya Luwalazi, koma padakali pano akumwa madzi aukhondo.

"M'dera langa ndikulimbikitsa ntchito zaulimi ndi za usodzi popeza anthu ambiri ndi asodzi ndi alimi," iwo atero.

Mu nthawi yawo ngati phungu, a Kondowe akuti akhazikitsa malo owonjezera ogulitsirako zipangizo zaulimi zotsika mtengo, akhazikitsa khoti pa Luwalazi, kumanga misika pa Chisenjere ndi Chamlame.

Iwo apempha anthu a m'deralo kuti awavoterenso kaamba koti akufuna agwirizane ndi boma poitanitsa makampani kuti adzayambitse ntchito za migodi m'deralo.

"Mogwirizana ndi aphungu anzanga tikufuna Nyumba ya Malamulo ikadutsitse lamulo lokhudza ulimi wa nzimbe ndi malonda a shuga chifukwa anthu a m'dera lino amalima kwambiri nzimbe.

"Likadzadutsa lamuloli, miyoyo ya anthu ambiri a m'dera lino idzatukuka. Kuyambira kalekale ulimi wa chamba umachita bwino m'boma lino. Choncho ndikabwerera ku Nyumba ya Malamulo ndidzayetsetsa kuulimbikitsa," atero a Kondowe.

Pothirirapo ndemanga, mkulu wa bungwe la Association of Persons with Albinism (APAM) a Maynard Zachariah ayamikira a Kondowe kaamba koimirira bwino anthu a m'dera lawo komanso anthu aulumali a m'dziko muno.

"A Kondowe si kuti ayimirira bwino anthu a m'dera mwawo mokha ayi, komanso anthu aulumali a m'dziko muno.

"Ndiyamikirenso anthu a m'dera la kumpoto chakumvuma kwa boma la Nkhota-kota kaamba kopereka mwayi woti munthu wa chialubino awayimirire," iwo atero.

A Zachariah akuti a Kondowe awonetsa kuti munthu waulumali atha kugwira ntchito yomwe walungalunga angagwire.

Iwo alimbikitsa anthu aulumali omwe akufuna kudzaimira kuti asagwe mphwayi, koma apikisane nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala.

Anthu aulumali omwe akufuna kudzaima nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala akuti a Overstone Kondowe, Clement Terence Chiwaya, Susan Chitimbe ndi George Claver ndiwo amawapatsa mangolomera ofuna kuimira madera awo.

A Emilia Chapaheya, womwe akudzaimira ngati phungu m'dera la kummwera chakumvuma kwa boma la Mulanje, afotokoza kuti ndale za a Chiwaya, Kondowe, Chitimbe ndi a Claver ndizo zidawalimbitsa mtima kuti atha kukwanitsa ndale.

"Anzathu adaimira madera awo ndipo adachita bwino kwambiri. Ichi ndi chilimbikitso chachikulu pa moyo wanga," adatero mayiwa womwe sakukaika kuti adzachita bwino.

A Umali Sungani, womwe akudzaimira ngati khansala ku Sankhwi ndi Mphamvu Kalima omwe akudzaimira ngati khansala m'dera la Nyamadzele ku Nsanje akuti ndale za a Chiwaya, komanso a Kondowe zimawasuntha kwambiri.

"Anthu amenewa amandilimbitsa mtima," atero a Sungani womwe akukhulupirira kuti adzachita bwino.



**Kondowe:** Munthu wa aulumali ali ndi kuthekera

# Alimbikitsa anthu aulumali kutenga gawo pa ndale

LOVEMORE KHOMO NDI BRIGHT KUMWENDA

Osaopa, osagwa mphwayi, osabwerera m'mbuyo!

Ichi ndi chilimbikitsa chomwe mabungwe a Federation of Disability Organisations in Malawi (FEDOMA) ndi a Association of Persons with Albinism (APAM) apereka kwa anthu aulumali omwe akufuna kudzaima nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala m'dziko muno.

Mkulu wa FEDOMA a Simon Munde apempha zipani za ndale kuti zitsatire mfundo za chitukuko za 2030 zomwe zimapereka mwayi kwa m'Malawi aliyense kuphakizirapo aulumali kutenga nawo gawo pa chitukuko komanso pa ndale.

Iwo akuti anthu aulumali ali ndi kuthekera kuchita bwino pa ndale ndi kutukula madera awo ngati wina aliyense.

"Zaka zapitazo tinali ndi a Clement Chiwaya womwe adali phungu waulumali wa m'dera lapakati la boma la Mangochi. Mkuluyu adachita bwino ndipo anthu a m'dera lake adamusankha kangapo kukhala phungu wa Nyumba ya Malamulo.

"M'mbuyomu anthu a ulumali aonetsa kuti ndale zawo n'zabwino, za chitukuko, komanso ndi zokonda anthu.

"Padakali pano a Overstone Kondowe akugwira ntchito yotamandika m'dera la kumpoto chakuzambwe kwa boma la Nkhotakota," atero a Munde.

Iwo akuti akhala okondwa kuona anthu ambiri aulumali akupikitsana nawo pa zisankho zikubwerazi.

Naye mkulu wa APAM a Maynard Zachariah alimbikitsa anthu aulumali kuti asagwe mphwayi kuimilira madera awo.

A Emilia Chapaheya, womwe akudzaimira ngati phungu ku Mulanje Pasani; a Umali Sungani womwe akudzaimira ngati khansala ku Sankhwi ndi Mphamvu Kalima womwe akudzaimira ngati khansala m'dera la Nyamadzele ku Nsanje ayamikira FEDOMA ndi APAM kaamba kowapatsa mangolomera.

"Mawu womwe a FEDOMA alankhula andilimbitsa mtima wofuna kukhala phungu wa Nyumba ya Malamulo," atero a Chapaheya.

Iwo akuti sabwerera mmbuyo ndipo akukhulupirira kuti adzachita bwino pa chisankhocho.

"Sindikukaika kuti ndidzachita bwino pa," iwo atero

A Sungani ndi a Kalima akuti a Kondowe, Chiwaya, Susan Chitimbe ndi George Claver ndiwo amawapatsa mangolomera ofuna kuimira madera awo.

"Anzathu adakwanitsa, ndili ndi chikhulupiriro choti inenso ndikwanitsa," atero a Kalima.

Kuphatikiza apo, mabungwewa akuphunzitsa maguluwa mmene angachitire kampeni, komanso akuwathandiza ndi zipangizo zochitira kampeni.

# Akhazikitsa ndondomeko zoletsa andale kukopa ovota ndi katundu

JOSEPH MWALE NDI BRIGHT KUMWENDA

Mkulu wa ofesi yoona m'mene zipani za ndale zimagwirira ntchito zawo, a Kizito Tenthani, akhala akukumana ndi atsogoleri a zipani za ndale komanso kuchititsa misonkhano n'cholinga choti Amalawi adziwe m'mene ndondomeko zoletsa andale kukopa ovota ndi ndalama komanso katundu zizigwirira ntchito.

Ofesi ya a Tenthani imalephera kugwiritsa ntchito lamulo loona za zipani kaamba koti idalibe ndondomeko.

Ndondomekozo adazisindikiza pa 23 Meyi patangotsala mwezi umodzi kuti bungwe la Malawi Electoral Commission (MEC) litsegulire nyengo yochititsa misonkhano yokopa anthu.

A Kizito adati ndondomekozo zikusonyeza kudzipereka kwa boma pofuna kuthana ndi mchitidwe wokopa ovuta ndi ndalama komanso katundu.



**Tenthani:** Tikufuna anthu adziwe za ndondomekozi

“Tikukumana ndi atsogoleri a ndale kuti adziwe za ndondomekozi ndi zimene tikuwayembekezera,” iwo adatero.

Lamulo loona za zipani limalola andale kupereka zovala za makaka a chipani chawo, zakudya komanso ndalama zoyendera kwa owatsatira.

Koma lamulo silikulola andale kupereka ndalama, katundu kapena mphatso zomwe cholinga chake ndi kukopa kapena kukakamiza anthu kuti awavotere pa zisankho.

Mkulu wa bungwe la National Initiative for Civic Education (NICE) Trust a Gray Kalindekafe apempha a Kizito kuti agwiritse ntchito ndondomekozo mosayang'ana nkhope.

Pothirirapo ndemanga pa nkhaniyi, mtsogoleri wa amayi a ndale m'dziko muno a Mary Thom Navicha akuti ndi wokondwa kuti tsopano ndondomekozo ziyamba kugwira ntchito.

“Ndine wokondwa kaamba koti amayi, achinyamata ndi anthu ena aulumali anali omangika kuchititsa misonkhano kaamba kosowa ndalama zopereka kwa anthu m'misonkhano yawo,” iwo atero.

Mneneri wa chipani cha Alliance for Democracy a Linda Limbe akuti ndondomekozo zithandiza kuchepetsa mavuto omwe andale amakumana nawo.

A Juliana Pasani a m'boma la Mulanje, a Joseph Zakariah a ku Dedza, Silvester Njikho a ku Nsanje, a Ganizani Mhango a ku Rumphi adati vuto ndi atsogoleri a ndale kaamba koti amangofuna kugwiritsa anzawo ntchito nthawi ya chisankho.

“Andalewa tikawaika m'mipando amatithawira n'kukakhala ku Blantyre kapena Lilongwe kutisiya ife manja ali mkhosi. Choncho timafuna tidyeratu zathu nanga si timawathandiza kuti alemere,” atero a Pasani.

Mabungwe a Oxfam ndi Women Legal Resource Centre (WOLREC) akhala akulimbana ndi mchitidwe wokopa anthu ndi ndalama komanso katundu kaamba koti umachititsa kuti amayi ambiri asapeze mipando.

“Ndale zokopa anthu ndi ndalama komanso katundu ndizo zikubwezera mmbuyo ntchito yoti pasakhale kusiyana pakati pa abambo ndi amayi pa ndale.

“Tikaunika tipeza kuti ndale zoterezi zimakomera abambo kaamba koti ndiwo amakhala ndi ndalama zokopera anthu poyerekeza ndi amayi, achinyamata ndi anthu aulumali,” atero mkulu wa Oxfam a Lingalireni Mihowa.

A Emilia Chapaheya, womwe akudzaimira ngati phungu m'dera la kummwera chakumvuma kwa boma la Mulanje, agwirizana ndi a bungwe la Oxfam ndi WOLREC.

“N'zoona ndalama zikumavuta,” iwo atero.

# Apempha zipani kusunga pangano

BRIGHT KUMWENDA

Amayi, achinyamata ndi anthu aulumali omwe akudzaima nawo pa zisankho za pa 16 Sepitembala apempha zipani zandale kuti zisunge pangano lomwe zidasaina ndi mabungwe a Oxfam ndi Women and Legal Resource Centre (WOLREC) pa bwalo la mfumu Nkanda m'boma la Mulanje chaka chatha.

Pa 24 Julaye, zipani za ndale zidalonjeza kulimbikitsa amayi, achinyamata ndi anthu aulumali kutenga nawo gawo pa ndale ndi kuwapatsa mwayi wochita nawo zisankho zachipulula.

A Hastings Mapundi, omwe akudzaima pa udindo wa phungu wa dera la pakati la m'boma la Nsanje komanso a Aida Adam Kunje, womwe akudzaima ngati khansala m'dera la Sankhwi ku Machinga, apempha andale kuti asunge phangano lomwe adasaina ndi mabungwe a Oxfam komanso Women Legal Resource Centre. (WOLREC).

Poyankha nkhaniyi mlembi wa chipani cholamula cha Malawi Congress Party (MCP) a Richard Chimwendo Banda, mu progalamu ya Mulimba, adati chipani chawo chikutsatira zomwe adasayinirana moti chidatsitsa ndi theka ndalama zomwe amayi amayenera kupereka kuti apikitsane nawo pa zisankho zachipulula.

“Mtsogoleri wa dziko lino a Dr Lazarus Chakwera amatsatira ndondomeko ya boma yoti mwa maudindo 40 pa 100 iliyonse azipita kwa amayi pamene abambo azitenga maudindo 60 pa 100 iliyonse.

“MCP ikuchita izi kuyambira posankha maunduna, komanso m'maudindo ake m'chipani.

“MCP ndi chipani chokhacho chomwe chili ndi amayi awiri omwe akutsatira kwa mtsogoleri wake a Lazarus Chakwera.

“A Abida Mia ndi wachiwiri kwa a Chakwera m'chigawo chakummwera pamene m'chigawo cha ku mpoto udindowu udapita kwa a Catherine Gotani Hara,” iwo adatero.



Atsogoleri a ndale kusaina pangano ndi mabungwe a Oxfam ndi WOLREC

Mlembi chipani cha Alliance for Democracy (AFORD) a Linda Limbe adati akutsatira panganolo ndi chidwi moti adasankha komiti yaikulu yoyendetsa ntchito za chipanicho momwe mamembala oposa 40 pa 100 iliyonse ndi amayi.

“Tikulimbikitsanso amayi, achinyamata ndi anthu aulumali kuti apikitsane nawo mu chisankho cha chipulula chomwe tichitise posachedwapa,” iwo adatero.

Mtsogoleri wa amayi mu Democratic Progressive Party (DPP) a Mary Navicha adati chipani chawo chikupititsa patsogolo miyoyo ya amayi, achinyamata ndi anthu aulumali pa ndale.

“Magulu atatuwa akulipira theka la ndalama zomwe anthu ofuna kupikitsana nawo pa zisankho za chipulula akupereka,” iwo atero.

Pologalamu ya Mulimba ikuuluka pa wailetsi ya kanema ndi chithandizo chochokera ku mabungwe a Oxfam ndi WOLREC.



**Navicha:** Ziwawa zimasokoneza

# Alonjeza kuthetsa ziwawa

BRIGHT KUMWENDA

Atsogoleri a ndale alonjeza kuthana ndi ziwawa zomwe zimachitika m'misonkhano ya ndale, povota komanso poulutsa zotsatira za zisankho.

Atsogoleriwa adapereka lonjezo lawo pa msonkhano womwe bungwe la Public Affairs Committee (PAC) lidachititsa posachedwapa mu mzinda wa Blantyre.

Pamsonkhanowo mneneri wa chipani cha Malawi Congress Party (MCP) a Jessie Kabwila adadzudzula mchitidwe wa ziwawa zokhudza ndale.

“Ziwawa ndi zolakwika posatengera kuti chipani chomwe chayambitsa ziwawazo chili m'boma kapena chilli mbali yotsutsa,” iwo adatero.

A Mary Navicha, phungu wa Democratic Progressive Party (DPP), adati chipani chawo chiyetsetsa kupewa ziwawa za ndale kaamba koti zikubwezera mmbuyo ntchito yolimbikitsa amayi kutenga gawo pa ndale.

“Amayi ambiri amaopa kulowa ndale kaamba ka ziwawa. Choncho ndipemphe apolisi kuti achitipo kanthu pofuna kuthana ndi mchitidwewu,” iwo adatero.

Alembi a zipani za MCP a Richard Chimwendo Banda ndi a DPP a Peter Mukhito m'misonkhano ya ndale akhala akudzudzula mchitidwe wa ziwawa.

Mlembi wa Alliance for Democracy (AFORD), a Linda Limbe, adati chipani chawo chimakhulupirira kuti nkhondo siimanga mudzi.

“Choncho tikulimbikitsa onse otsatira AFORD kuti apewe ziwawa chifukwa ndale si kuchitira ena za mtopola,” iwo atero.